Kafukufuku wa

ULAATIBU

(Mwambo wa Kukwera kwa Khatweeb pa Minbar ya Jum'ah)

Poyerekeza ndi Chiphunzitso cha Mtumiki wathu Muhammad salla Allah alaih wasallam

Ofufuza:
Ramadhan Nu'man AbuBakr Isa
www.malawiummah.com

Makolo athu omwe tinawapeza akuchita zomwe lero lino timaziona kuti zinali zosalondola, tiziwapemphera zabwino za Allah kuti awachitire chisoni ndi kuwaika malo a Mtendere, poti anali kuchita zimenezo ndicholinga chabwino, kuti Deeniyi tiipeze ili yolimba. Munthawi zawo makolo kunalibe ilm yokwanira ndipo kupeza maphunziro a Deen kunali kovutikira, kusiyana ndi masiku ano pamene munthu akukwanitsa kupeza ilm kudzera pa phone ali chikhalire mnyumba mwake. Allah awadalitse makolo athu omwe anali kutha mitunda itali-itali, kusakasaka maphunziro a Deen. Inde, anali kumanidwa ufulu wa kuphunzira mmasukulu chifukwa cha kugwiritsa Chipembedzo chawo, ndipo kwawo kunali kufalitsa Deeniyi.

Lero lino Alhamdulillah kwa amene Allah anawafewetsera, akumatha kufikira maphunziro omwe makolo athu sanawafikire, omwe mkati mwakemo muli chiwongoko chenicheni cha mu Deen. Ndipo akumatha kusiyanitsa pakati pa zoona ndi zabodza, kuchokera mu Qur'an ndi Sunnah komanso mmabuku omwe anali kulembedwa kalekale, zomwe ma ulamaa ena anazikhonza pambuyo pa kafukufuku osiyanasiyana. Alhamdulillah. Choncho lero lino, ndizofunika kwaife kupewa zopeka ndikutsatira zoona, ndipo tisakakamire zopeka pambuyo poti tazindikira chifukwa choti anali kuchita makolo athu. Pa izi, Allah Ta'ala akutilangiza kudzera mwa anthu akale omwe anali kuchita makani pamene Mtumiki salla Allah alaih wasallam anali kuwaongolera pambuyo poti amira mzikhalidwe za makolo zosemphana ndi Chislamu. Akunena kuti:

﴿وَإِذَا قِيلَ لَهُمُ ٱتَّبِعُوا۟ مَآ أَنزَلَ ٱللَّهُ قَالُوا۟ بَلْ نَتَّبِعُ مَآ أَلْفَيْنَا عَلَيْهِ ءَابَآءَنَآ ۚ أَوَلَوْ كَانَ ءَابَآؤُهُمْ لَا يَعْقِلُونَ شَيْـًٔا وَلَا يَهْتَدُونَ ﴿١٧٠﴾﴾

"Ndipo kukanenedwa kwa iwo (kuti): "Tsatirani zimene Allah wavumbulutsa;" Akunena: "Koma tikutsata zimene tidawapeza nazo makolo athu." Kodi ngakhale kuti makolo awo sadali kuzindikira chilichonse ndiponso sadali oongoka (awatsatirabe)?"[1]

[1] Surah Al-Baqarah 170

Tisatsate zomwe tikuzidziwa kuti ndizolakwika mu deen pachifukwa choti tinawapeza nazo makolo athu, koma mmalo mwake tiziwapemphera chikhululuko ndi zabwino makolo athuwo, ife natitsata zabwinozo.

Kuchokera muchiphunzitso cha Mtumiki salla Allah alaih wasallam, pamene Khatweeb akukwera pa minbar azikwera mwapang'onopang'ono, ndipo akamatsika azitsika mofulumira pofuna kulumikiza khutbah ndi swalaat.[1]

Zomwe zinakhanzikika kumadera ena ndizoti ma Khatweeb ena amati akamakwera pa minbar amayenda mwapang'onopang'ono pambuyo pa Muadddhin yemwe amakhala akulakatula mawu asanakwere pa minbar, komanso akakwera, asanayambe Khutbah pambuyo pa Adhan. Zimenezo zikusemphana ndimmene anali kuchitira Mtumiki salla Allah alaih wasallam. Ndipo ma ulamaa ena anaziika m'gulu la bid'ah, monga mmene ananenera Abu Shamaah mu "Al-Ba'ith p.224", komanso Al-Qasimi mu "Islaahil Masaajid p.48" ndi ena.

Palinso zichitochito zina monga imaam kugogoda ndi ndodo katatu pa minbar molimbika pamene akukwera, monga mmene analongosoleranso mu "Al-Ba'ith p.224", Rawdhwatu Taalibeen vol.2/32 ndi Islaah Al-Massajid p.48 ndi ena.

[1] Al Furoo' 2/129

ULAATIBU

Tatiyeni tione ndondomeko yomwe imachitika mmizikiti ina, munthawi imene Khatweeb akupita pa Minbar, ndondomeko yomwe imatchedwa kuti *Ulaatibu*. Ndipo tiona kuti kodi malamulo a Khutba akuti bwanji pa *Ulaatibu*?

Muaddhin amanyamula buku la Khutbah ndi ndodo ija yomwe ma Khatweeb ena amagwirizira pa Khutbah, amaiyika pampata wa zala ziwiri zoyambilira kuphazi lamwendo wamanzere. Ndipo anthu amapanga kanjira kodutsamo Muadhin atatsogozana ndi Khatweeb, kenako amayamba kulakatula izi (ali chiimire):

السلام عليكم ورحمة الله وبركاته

إن الله وملائكته يصلون على النبي - يا أيها الذين آمنوا صلوا عليه وسلموا تسليما - يبشرهم ربهم برحمة منه ورضان، وجنات لهم فيها نعيم مقيم، خالدين فيها أبدا، إن الله عنده أجر عظيم.

Ndipo akangomaliza mawu amenewa, amanyamula mwendo, kuyambika kwa ulendo waku Minbar. Kenako amanena kuti:

اللهم يا حنان يا منان

Kenako amaponya step kupita kutsogolo,,

اللهم أعز الإسلام والمسلمين

Pamenepo amaponyanso step ina mwendo kupita kutsogolo,,

وأذل الشرك ورالمشركين

Ndipo amaponya step ina kupita kutsogolo,,

ذلك تقيم إلى يوم الدين

Step ina kupita kutsogolo,,

برحمتك يا أرحم الرحمين

Pamenepo ndiye kuti afika pa Minbar

Ndipo Khatweeb amakhala akutsatira mbuyomu step by step. Akafika pafupi ndi minbar, Khatweeb amamudutsa muaddhinuyu ndikupita kutsogolo, kukakwera pa minbar ndikupereka salaam. Akamaliza kupereka salaam, amalandira ndodo ija pamodzi ndi Khutbah (kawirikawiri khutbah yake imakhala ya Ibn Nabaatah[1]) ndikukhala pansi, kudikira Adhaan. Kenako Muadhin akamaliza Adhan, Khatweeb amapanga Dua ya pagulu. Akangomaliza Dua imeneyi, Muadhin amapitiriza kulakatula mawu awa:

روي في خبر عن أبي هريرة رضي الله عنه قال: قال رسول الله صلى الله عليه وسلم: "إذا صعد الخطيب المنبر فلا أحد يتكلم، ومن تكلم فقد لغى، ومن لغى فلا جمعة له" – اسمعوا وأنصتوا يرحمني ويرحمكم الله

Kenako amakhala pansi ndipo Khatweeb amayamba Khutba yake. Kodi malamulo a Khutbah akuti bwanji pa ndondomeko imeneyi?

Choyamba, Hadith yomwe yatchulidwayo ndiyoona ndithu, ngakhale kuti inabwera mosiyanasiyana mawu ake, koma ikuchokera mu Sahih Al-Bukhari pamutu wa Al-Jum'ah, khomo la 46, number 394, komanso Sahih Muslim vol.2/583, number 851. Komanso Aayah yomwe yatchulidwayo ndi ya m'Surah Al-Ahzaab, number 56. Zonsezi ndizabwinobwino ndithu, ndipo muli malamulo ofunikira tsiku la Jum'ah; monga kuwalamula anthu kuti amfunire zabwino Mtumiki Salla Allah alaih wasallam ... ndizofunikira tsiku la Jum'ah. Koma nthawi yowauzira anthu ndi mauzidwe akewo, ndi imene siikugwirizana ndi Malamulo a Jum'ah. Mawuwa amawamva okhawo omwe akumva chiyankhulocho. Komanso malo ndi nthawi zake sizimenezo, chifukwa choti zikusemphana ndi mmene aliri malamulo a makweredwe a Khatweeb pa minbar.

Pankhani ya kulakatula mawu ndikumamuperekeza Khatweeb pa minbar, Imaam Abu Al-Abbaas Taqiyu Ddeen Ahmad bun Abdil Haleem Al-Harraan Al-Dimashqi Al-Hanbali, Sheikhul Islam Ibn Taymiya, atafunsidwa anayankha kuti: *"Alhamdulillah, zimenezo sizikuchokera mu Sunnah za Mtumiki salla Allah alaih wasallam, komanso palibe mmodzi mwa ma Imaam a Chisilamu omwe anaziloleza.*

[1] Ibn Nabaatah ndi chitabu cha ma Khutbah, chomwe chinalembedwa ndi Abdul Rahim bun Muhammad bun Nabaatah, yemwe anabadwira ku Syria mchaka cha 335H ndikumwalira mchaka cha 473H

Koma ndinjira yokhayo yomwe anthu ena anasankha kuti azigwiritsa ntchito pofalitsa uthenga wa kukhala chete apmene Khutba ikuchitika"[1].

Tsopano ndodo yomwe amayenda nayo muaddhin ndikum'patsira Khatweeb pa minbar, zimenezi zinachokera muchikhulupiliro chonena kuti Mtumiki salla Allah alaih wasallam anali kunyamula ndondo pa khutbah. Zoona zake tizipeza mu buku la Zaadul Ma'adi fi Hadyi Khayril Ibaad, p.414, pamene Imaam Ibn Al Qayyim akunenetsa kuti:

ولم يكن يأخذ بيده سيفا ولا غيره.

"Ndipo (Mtumiki) sanali kutenga mmanja mwake lupanga kapena chirichonse." Sanali kutenga ndodo kapena lupanga nthawi zonse, monga momwe ena amaganizira ndikumafalitsa, kuti Mtumiki anali kunyamula lupanga pa minbar kumadera omwe Chisilamu chinalowa ndi lupanga, pomwe kumadera omwe Chisilamu chinalowa ndi mawu okha, sanali kunyamula. Izi maulamaa anati zilibe umboni, komanso chilungamo chake ndichoti Chisilamu sichinafale ndi lupanga, ndipo zikanenedwa choncho zimapereka chithunzithunzi choti Chisilamu chinafala ndi lupanga.

Ndisunnah kuyezamira ndodo, ndipo izi zikuikiridwa umboni ndi ma imaam a madh'hab a Malik[2], Shaf'i[3] ndi Hanbal[4]. Maumboni amenewa ndiamphamvu kuposa maumboni omwe anabweretsedwa ndi Madh'hab a Abu Hanifa[5], makamaka Hadith ya Al-Hakam bun Huzn yomwe ma ulamaa ena owunika ma Hadith monga Imaam Al-Nawawi ndi Ibn Al-Hajar, anaitchula kuti ndiyabwino (hasan. Komanso Sheikh Muhammad bun Ibrahim Aali Sheikh anaikira ndemanga Hadithiyo, kunena kuti "mmenemo muli kulolezedwa kwa kuyezamira ndondo kapena chinachake pa khutba, kuti munthu alimbe mmaimidwe ngati angatope nthawi ina. Ndipo kupanga choncho ziri Sunnah ndithu. Inatchulidwa ndodo chifukwa choti ndiyomwe inali

[1] Majmu'ul Fatawa vol.22/217
[2] Al-Mudawwanah vol.1/156, Al-Bayaan wa Tahsweel vol.1/341, Mawaahibul Jaleel vol.2/172, Sharh Swagheer vol.1/181 ndi Al-Fawaakih Ddawaani vol.1/307
[3] Al-Umm vol.1/230, Al-Haawi vol.3/53-54, Al-Wajeez vol.1/64, Al-Majmoo' vol.4/528, Rawdhwat Taalibeen vol.2/32 ndi Mughni Al-Muhtaaj vol.1/290
[4] Al-Hidaayah (Abu Al-Khatwaab) vol.1/52, Al-Mughni vol.3/179, Al-Furoo' vol.2/119, Al-Muharrir vol.1/151, Al-Inswaaf vol.2/397 ndi Al-Mubdi' vol.2/163
[5] Haashiet Al-Tahtaawi alaa Muraaqil Falaah p.334

kukhala chifupi ndi Mtumiki salla Allah alaih wasallam, monga mmene ndodo imakhalira chifupi ndi anthu lero lino.” Choncho ndizololedwa kuyezamira pachinachake monga ndodo kapena chipilala cha minbar ngati ochita khutba walema ndipo sakwanitsa kuima moongoka[1]. Koma asatenge ndondo kukhala chimodzi muzinthu zogwiritsa ntchito pa khutbah popanda chifukwa.

Kuchokera mu Al-Muntaqaa min Fataawa Sheikh Al-Fawzaan vol.2/178, anatiyankhiramo funso, pamene ofunsa anafunsa kuti:

Kwathu kuno Imaam akakwera pa minbar tsiku la Jum’ah, ochita Adhaan amaima nkupanga adhan, kenako molimbika amabweretsa Hadith yoti Mtumiki salla Allah alaih wasallam anati:

إذا صعد الخطيب المنبر فلا أحد يتكلم، ومن تكلم فقد لغا، ومن لغا فلا جمعة له، اسمعوا وأنصتوا يرحمني ويرحمكم الله

Kodi lamulo likuti bwanji pa zochita zimenezi?

Sheikh anayankha kuti: kupanga zimenezo ndi bid’ah. Chifukwa ndi ntchito yomwe Mtumiki salla Allah alaih wasallam sanachite. Ndizoona kuti Mtumiki analetsa kuyankhula nthawi ya khutbah ndipo anati kuyankhulako ndi masewera, kutanthauza kuti zimaononga swalaat. Koma zoti mawuwa aziyankhulidwa Khatweeb asanayambe khutba, zimenezo sitikuzidziwa M’chisilamu.

Palibe dua yomwe imayenera kunenedwa pamene Khatweeb akukwera pa minbar, komanso asanakhale pansi kuti Adhaan ichitike (zomwe madera ena amazitcha kuti *ulaatibu*). Koma zimenezi ndizina mwa zopeka zomwe madera ena amachita.

Ena mwa omwe anatsimikiza zoti *ulaatibu* umenewu muchiphunzitso cha Mtumiki mulibe, ndi ma Imaam a madh’hab a Shaafi’i (Al-Majmu’ 4/529, Rawdhatu Taalibeen 2/32, Mughni Al-Muhtaaj 1/290), ma Imaam a madh’hab a Hanbali (Al-Furoo’ 2/125, Kashaaful Qannaa’ 2/37), komanso Sheikhul Islam Ibn Taymiya (Al-Ikhtiyaaraat p.80) ndi ophunzira wake, Ibn Al-Qayyim (Zaadul Ma’adi 1/189, 429).

[1] Fataawa wa Rasaail vol.3/21

Mu Al-Ikhtiyaaraat ananena kuti: Dua ya Imaam pambuyo pa kukwera kwake pa minbar ilibe phata m'Chisilamu.

Tikhona kuwonjezeranso zambiri zokhudza Khutba, powerenga buku lotchedwa Khutbatul Jum'ah wa Ahkaamuhal-Fiqhiyyah, lolembedwa ndi Abdul Aziz Al-Hujailaani, komanso mu Al-Shaamil fi Fiqhil Khatweeb wal Khutbah, lolembedwa ndi Sheikh Su'ud Al-Shuraym.

Chidule cha zonsezi, Mtumiki salla Allah alaih wasallam akafuna kupanga Khutbah pa Jum'ah, anali kukwera pa minbar popanda kuyankhula kalikonse, kenako Bilaal radhia Allah anhu anali kuchita Adhan ndipo sanali kuwonjezera mau aliwonse. Nthawi zina ankayezamira ndodo yake yomwe inali kumuthandizira nthawi zonse akalema nkuima, koma sanaipange ndondoyo kuti izipezeka munzikiti ngati imodzi mwa nsichi za Khutbah. Mtumiki salla Allah alaih wasallam akamaliza kupanga Khutbah, Bilaal anali kupanga iqaamah.

Allah Ta'ala ndiye Mwini kudziwa konse